# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA ZOMBA M'DZINJA LA 2024-2025

## NYENGO YA DZINJA LA 2024/2025 MWACHIDULE

Nyengo ya dzinja ya 2024/2025 ikuyembekezereka kukhudzidwa ndi La Nina wochepa mphamvu. La Nina ndi kuzizira kwa madzi mdera la pakati chakum'mawa kwa nyanja yamchere ya Pacific. Izi zikhala chomwechi mpaka kumayambiriro a chaka cha 2025


Boma la Zomba likuyembekezereka kulandira mvula pa **mlingo wokhazikika komaso wocheperako pa mlingo wokhazikika miyezi ina.**

## October 2024





Boma la Zomba mu mwezi wa October likuyembekezereka kulandira mvula yochepa ndipo madera ena adzalandira mvula koma yosapitilira mlingo wa 50mm. Pali chiyembekezo cha mvula ya Chizimalupsa yomwe izabwere ndi chiopyezo cha mphepo ya nkuntho komanso ziphaliwa

## November 2024





Mvula ya mlingo wa pakati pa 50mm – 100mm ikuyembekezereka mu mwezi wa November. Madera ambiri mu bomali akuyembekezereka kulandira mvula yodzalira pakati pa sabata ya chitatu ndi yachinayi ya mwezi wa November.
Pali chiyembekezo chakuti mvula yi itsagana ndi mphepo yowononga komaso ziphaliwali.

## December 2024




Madera ambiri mu Zomba akuyembekezereka kudzalandira mvula pakati pa mlingo wa 150mm ndi 250mm mu mwezi wa December.
Madera ena a kwa TA Mkumbira komaso TA Mwambo atha kudzalandira mvula ya mlingo wocheperako pakati pa 100mm-150mm komaso mvula yochepera 100mm mu mwezi


## January 2025




Mwezi wa January ukuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo pakati pa 200mm ndi 300mm. Madera ochepa mdera la TA Mwambo ndi SC Mbiza atha kuzalandira mvula yochepera mlingo wa 200mm.

Madera ena mdera la TA Mwamba atha kukhala ndi ng'amba masiku osaposera sabata


## February 2025




Mwezi wa February, madera ambiri akuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo wa pakati pa 150mm ndi 250mm.

Pali kuthekera kwa ng'amba mdera la TA Mwambo komaso madera ena mdera la Chikamveka kwa masabata osapitilira awiri.


## March 2025




Mu mwezi wa March, madera a Chikamveka komaso Chambo akuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo wa 200mm ndi 250mm.

Mvula ya mlingo wa pakati pa pa 150mm ndi 200mm ikuyembekezereka mu madera ambiri mu bomali.


## April 2025




Mwezi wa April ndi mwezi womwe dzinja limathera mu boma li.
Madera ena ozungulira TA Malemia, Chikamveka ndi Chambo akuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo pakati pa 100mm ndi 150mm.
Madera ambiri akuyekembekezereka kudzalandira mvula yosapitilira 100mm mu mwezi wa April.

*Pali Chiyembekezo chakuti mvula yobzalira idzagwa pakati pa sabata yachitatu ndi yachinayi ya November. Pofika msabata yomaliza ya March kapena sabata yoyambilira ya April. Nyengo ya dzinja idzakhala ikufika kumapeto. Kutalika kwa dzinja kukuyembezereka kukhala ma masiku* ***a*** *pakati pa* ***120 ndi 140.*** *Miyezi ya January ndi February pali chiyembekezo chachikulu chokhala ndi ng'amba koma yosapitilira masabata awiri m'bomali*

| ZOMBA | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 3.7 | 30.5 | 13.6 |
| NOV | 64.4 | 104.2 | 67.1 |
| DEC | 198.7 | 291.9 | 259.9 |
| JAN | 232.5 | 381.3 | 360.2 |
| FEB | 181.1 | 299.0 | 283.5 |
| MAR | 124.1 | 222.9 | 231.5 |
| APR | 27.7 | 70.1 | 48.5 |




**Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2024**

**Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:**
The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw

Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku: